

MARKING KEY- CHICHEWA PAPER 1

Gawo A: (Malikisi 40)

Chimangirizo kapena kalata

Malangizo

1. Yankhani funso **limodzi** lokha mgawo ili. Musatenge ola limodzi ndi mphindi khumi poyankha funsoli.
2. Lembani chimangirizo kapena kalata pa masamba **4** mpaka **7**. Mawu a m'chimangirizo **kapena** kalata osachepera **300** koma asapitirire 400
3. Malikisi adzaperekedwa pakayalidwe ka chimangirizo kapena kalata, mfudo ndi kgwiritsedwe tchito koyenera ka nsinjiro za chiyankulo.

1. a. Lembani chimangirizo pa mutu uli munsimu:

Kusintha kwa chikhalidwe cha Amalawi m;nyengo ya matenda a Covid-19 (Malikisi 40)

➤ Kasamalidwe ka matenda

- i. Anthu adayamba kuvala zotchingira pakamwa ndi mphuno podwazika matenda
- ii. Wodwala amayikidwa m;chipinda chayekha mpaka atachira
- iii. Anthu akapatsidwa mphindi zotchepa kuti azonde wodwalayo

➤ Pamaliro

- i. Anthu samakhala pa siwa monga achitira nthawi zonse
- ii. Maliro a munthu yemwe amadwala Covid-19 amayikidwa ndi azaumoyo

➤ Kuzonda achibale/kuchezerana

- i. Anthu sadali omasuka kukazonda kapena kuchezerana ndi achibale



ii. Anthu samampatsana moni wapamanja ndi achibale

➤ Pamalo osiyanasiyana

i. Anthu amakhala motalikirana pamalo

ii. Anthu samaloledwa kukhala m'magulu a anthu ambiri pamalo

iii. Kuchita misonkhano kunali koletsedwa pamalo ena

iv. Malo ena datsekeda monga malo a sukulu ndi achisangalalo

➤ Ukhondo wa munthu

i. Anthu adayamba chizolowezi chosamba m'manja ndi sopo kapena sanitaizi mowirikiza

ii. Anthu amayenda atavala zotchinga pakamwa ndi mphuno

KAPENA

b. Lembani kalata kwa mfumu yaikulu ya m'dela lanu yomufotokozera kuipa kokhulupirira kuti munthu wokalama ndi mfiti

➤ Munthu weokalama sapisidwa chisamaliro chokwanira

i. Samapatsidwa chakudya chokwanira

ii. Samasamalidwa akadwala

iii. Samasambitsidwa

➤ Amakhala ndi mantha komanso nkawa

i. Amakhala mosamasuka kapena mocheukacheuka kuopa anthu ena

ii. Amakahala m;maganizo osiyanasiyana achimene chingamuchitikire iye nyengo ina iliyonse

Mafunso akupitirira/...



- Atha kuchitidewa chipongwe
 - i. Atha kumenyedwa kapena kuphedwa kumene
 - ii. Atha kunyozedwa ndikusapatsidwa ulemu

- Amakanizidwa kutenga nawo gawo muzinhu zambiri
 - i. Sapatsidwa mwai olandira nawo zithandizo zosiyanasiyana zochokera ku boma ngakhale kwa anthu akufuna kwabwino
 - ii. Satenga nawo gawo m'zochitika za ku dera ndi mpingo

- Amathamangitsidwa m'mudzi
 - i. Amalamulidwa kuti asamuke ndi kukhala dera lino osati la kwawoko
 - ii. Amalamulidwa kusamuka ndi kukakhala paokhaokha m'deralo

KAGAWIDWE KA MALIKISI

- ✓ **Kalembedwe – malikisi 3**
- ✓ **Mfundo zisanu – malikisi 25**
- ✓ **Malamulo a chiyankhulo – malaikisi 7**
- ✓ **Nsinjiro zachiyankhulo – malikisi 3**

GAWO B (Malikisi 20)

Yankhani mafunso onse a mgawoli.

2. Werengani malonje olembedwa m'munsimu ndipo muyankhe mafunso otsatirawo pa mizere ili pansi pa funso lililonse

“Anzathu, ife takulandirani ndi manja awiri. Uwu tayambawu ndi ubale. Kachipsolopsolo takulandiraninso ndi manja awiri. Msoti wathu mwauona, ndiopanda chilema chilichonse. Tikhulupirira mudzatisamaliranso. Sitidakupatseni wachitopa ayi. Chiwongo chake ndi nkuku zisanu kapena K25,000.00

a. i. Kodi malonje ndi a mtunduwanji?

✓ Malonje a paukwati **(Malikisi 1)**

ii. Nanga akuyankhula m'malonjewa ndani? **(Malikisi 1)**

✓ Ankhoswe akuchikazi/khoswe yakuchikazi/malume ake a mkazi

iii. Tchulani nthawi yomwe malonjewa angachitike? **(Malikisi 1)**

✓ Nthawi yomanga chinkhoswe/nthawi yotula mbeta

iv. Ndi mawu ati m'nkhanayi omwe akusonyeza kuti anthuwa asayinirana pangano lamgwirizano.

✓ Uwu tayambawu ndi ubale.

(Malikisi 2)

b. Perekani matanthauzo a mawu ali m'munsimu monga agwiritsidwa ntchito m'malonjewa

i. Kachipsolopsolo

✓ Mnyamata yemwe wafika msinku wokwatira **(Malikisi 1)**

ii. Msoti

✓ Msikana yemwe wafika msinkhu wokwatiwa **(Malikisi 1)**

iii. Wachitopayo ayi

✓ Wosadwala konse/wamphamvu ndithu **(Malikisi 1)**

iv. Chiwongo

Mafunso akupitirira/...



✓ Malipiro omwe akuchimuna amapereka pofunsira mbeta (Malikisi 1)

d. Perekani malangizo **atatu** omwe mungapereke kwa mzanu yemwe sakusamala ntchito

i. Atha kuchotsedwa ntchito (Malikisi 1)

ii. Ntchito ikatha adzazunzika pamodzi ndi omudalira onse. (Malikisi 1)

iii. Akhonza kumasemphana maganizo ndi omulemba ntchito. (Malikisi 1)

iv. Zingabweretse udani pakati pa iye ndi omulemba ntchito. (Malikisi 1)

v. Akhonza kumasalidwa pa zochitika zina ndi akuluakulu pantchitopo.

(Malikisi 1)

d. Perekani njira **zitatatu** zofalitsira uthenga wa kasamalidwe ka zachilengedwe kewa anthu a m'mudzi

i. Kudzera pa msonkhano

ii. Kudzera pa wailesi

iii, Kukhoma zikwangani

MAYANKHO ATHERA PANO